**SPEECH**

**BY**

**HIS EXCELLENCY**

**DR. LAZARUS MCCARTHY CHAKWERA,**

**PRESIDENT OF THE REPUBLIC OF MALAWI**

**AND PRESIDENT OF**

**MALAWI CONGRESS PARTY**

**AT**

**THE NORTHERN REGION LAUNCH**

**OF THE MALAWI CONGRESS PARTY**

**2025 CAMPAIGN**

**MZIMBA STADIUM**

**MZIMBA, MALAWI**

**19TH APRIL 2025**

**Kwacha!**

**Kwacha!**

**Boma!**

**Boma!**

---

**Amayi ndi Abambo,**

**Pamene tafika kuno ku Mzimba ndiye kuti kampeni yayambika. Ndipo ine chitsekulire kampeni yanga loweruka ku Lilongwe, ndinawauziratu akuluakulu achipani kuti koyambilira kupitako kukapanga kampeni kukhale ku Mzimba, chifukwa kuno mchaka cha 2020 omwe munandivotela ndi anthu ochuluka, mpaka munakwana 287,488. Ndiye zoona zake nzoti ineyo lero ndine Pulezidenti wa Malawi chifukwa inu anthu a ku Mzimba munandivotera mwamkokomo. Komanso kuno ku mpoto amene munandikhulupilira kukhala Pulezidenti wanu ndi ambiri, chifukwa olo inu a ku Chitipa, munandivotela anthu 50,277; inu aku Karonga munandivotela anthu 74,665; ku Likoma munandivotela anthu 2,981; ku Nkhatabay munandivotela anthu 45,591; pamene ku Rumphi munandivotela anthu**

**55,153. Ndiye kuti tikaphatikiza nambala ya anthu kuno kumpoto amene voti yanu ndiyomwe inandikhazikitsa boma liripo leroli, mukukwana 516,155. Ndiye ngati muli mmodzi wa anthu amene munandivotela mu 2020, boma ndikuyendetsa leroli silanga ayi, koma lanu. Ndipo wina asazakunamizeni kuti voti yomwe munandipatsa siinagwire ntchito, chifukwa zomwe bomali lachita mdziko muno muzaka fayifi zapitazi ndi ntchito za voti yanu.**

**Oti mukamaona kuti pa Mzimba boma pano pamangidwa Stadium yomwe yatsala pang'ono kutha, yamanga ndi voti yomwe munandipatsa. Mukamaona kuti Mzuzu Youth Centre yomwe inkakanika kuyamba mmbuyomu inayamba kumangidwa, yachita zimenezo ndi voti yomwe munandipatsa. Mukamaona kuti makomo oposa 100,000 ku Nkhatabay ndi ku Rumphi ayamba kupeza madzi apampopi, yabweretsa madziwo ndi voti yomwe munandipatsa. Mukaona kuti nseu wa M1 ofikira kuno ku mpoto kuchokera ku Lilongwe ukukonzedwa mwamakono, ikukonza nseuwo ndi voti yomwe munandipatsa. Mukaona kuti mabwalo a ndege ku**

**Mzuzu ndi ku Karonga akonzedwa nkuyamba kulandira ndege zikuluzikulu, yachita ntchito imeneyo ndi voti yomwe munandipatsa. Olo mabanja okwana 72,022 kuno ku mpoto omwe mwalandila chakudya kuti chikuthandizeni mmene minda yanu inaonongeka ndi ngozi ya nyengo, chinakubweretserani chakudyacho ndi voti yanu yomwe munandipatsa. Olo mabanja omwe mwakhala mukulandira chithandizo cha ndalama ya mtukula pakhomo, kapena feteleza wa AIP, yakufikitsa chithandizocho pakhomo lanu ndi voti yomwe munandipatsa. Olo library yamakono yomwe ndikumanga ku Mzuzu University, ikumangitsa ndi voti yomwe munandipatsa. Olo Quota System yomwe ndinathetsa pa masankhidwe a ana askulu kuno, inandipatsa mphamvu zothetsera ndi voti yomwe munandipatsa. Olo nduna ndi akuluakulu ena aboma ochokera kuno ku mpoto omwe ndinawaika mmipando ikuluikulu kuti chigawo chakumpoto chikhale mkati mwenimweni moyendetsa boma, inandipatsa kuthekera yowaika mmipandoyo ndi voti yomwe munandipatsa. Olo anthu 63,000 kuno ku mpoto omwe alandira ngongole za NEEF zokwana 54 billion, ma bizinesi 63,000 atsopano amene ayambika kuno ku mpoto**

**ayamba chifukwa cha voti yomwe munandipatsa. Komanso anthu omwe abweza ngongole za NEEF kuno kumpoto chifukwa mabizinesi awo anagwira nseu anakwana 86%, the highest repayment rate of any region, which means kuti mu second term yanga ndalama yabwezedwayo ifikiranso ena kuti nawo athandizidwe nawo. Zonsezi zachitika chifukwa cha voti yomwe munandipatsa kuno ku mpoto.**

**Ndiye kampeni yanga chaka chino siikuchulutsa zonena ngati ya anthu otsutsa boma. Kampeni yanga ndiyongokupemphani kuti voti yomwe munandipatsa mu 2020 kuti iyambe zitukuko zomwe pano zili mkati, mundipatsenso pa September 16 kuti tipititse chitukuko chanu patsogolo. Kampeni yanga ndiyongokupempha kuti chikhulupiliro chomwe munali nacho pa ine mu 2020 musachitaye tili pakati pa nyanja nkudumphira mmadzi omwe atakokolole zonse zomwe tayambazi mmalo momalizitsa. Kampeni yanga ndiyokupemphani kuti tipitilize kuyenda pamodzi mpaka tikafika komwe tikupita, chifukwa komwe tikupitaku kuli zokomela tonse. Mu Manifesto yathu ya**

**2020 tinaika zambiri zomwe tapanga, monga mmene mwamvera ena akufotokoza pano, koma popeza ulendou ndi wa zaka teni mpaka 2030, ndikupempha kuti voti yanu mundisungire kuti ndimalize ntchito zatsalazo, chifukwa kaya ndi Airport yatsopano ku Mzuzu, kaya ndi Mmbelwa University, ndalama zama projekti amenewa ngakhale zinachedwa kuzipeza, mmene tazipezamu ndiye kuti ntchitoyono tiigwira ndithu mu second term yanga. Komanso sizokhazo, chifukwa pano takunganso Manifesto yatsopano yomwe taikamo zomwe tikufuna tichite kuno ku mpoto kuti tipititse chitukuko chanu patsogolo.**

**Mu Manifesto imeneyi taikamo nsanamira fayifi zomwe takonza kuchita. Yoyamba ndi Food Security, yomwe cholinga chake ndi Chakudya Chofikira Aliyense. Mfundo imenei muimvetsetse. Situkunena kuti Chakudya chokwanira aliyense, koma chofikira aliyense, chifukwa muzaka fayifi zimenezi takhala tikulima ndi kukolola chakudya chokwanira aliyense mdziko muno, koma vuto ndi loti chakudyacho sichikumafikira aliyense. Izi zikumachitika pa zifukwa zingapo, monga**

**kusowa kwa ma storage facility osungira zokolola zanu, zomwe zikupangitsa kuti chakudya chambiri chizionongeka. Ndiye mu Manifesto yanga muli mfundo zomanga ma storage a chakudya mmaboma onse kuti chakudya chizifikira aliyense. Ndipo ma storage facility ena tayamba kale kumanga, koma kunonso ku mpoto tionjezera. Ndiye mu Manifesto yanga muli mfundo yopereka mpata kwa nonse omwe mumalima chakudya chochuluka kuti muzitha kupereka chakudya cha surplus ku National Food Reserve mmalo mopereka misonkho ina. Komanso chifukwa china chomwe chakudya sichifikira aliyense ndi dyera ya anthu ena ogwira ntchito yogulitsa ndi kugawa chakudya. Ndiye mu Manifesto yangayi muli mfundo yosintha kayendetsedwe ka ntchito yogulitsa ndi kugawa chakudya kuti chizifikira aliyense. Chifukwa china chomwe chakudya sichifikira aliyense ndi choti achinyamata ndi azimayi ambiri mulibe minda yanu yanu ya nthaka yabwino yoti muzilimapo chakudya. Ndiye mu Manifesto yangayi muli mfundo yopereka minda kwa achinyamata ndi azimayi yomwe mutha kugwiritsa ntchito ngati collateral yokapezela ngongole ku NEEF kuti muchite ulimi wa zakudya mwakathithi.**

**Mwinatu ena simukudziwa kuti za chakudyazi ndiri nazo siriyasi. Panopa alimi okwana 50,000 ndawapatsa kale ndalama zokwana 20 billion kuti apange winter cropping, ndipo alimiwa alima minda yokwana 100,000 acres ya zakudya chomwe titakolole kumapeto kwa mwezi wamawa. Zoti mdziko muno muzikhala chakudya chosakwana ndati sindilola, chifukwa ndikhala ndikupitiliza kutukula ulimi mpaka tikhale dziko lodzidyetsa lokha chaka chonse.**

**Nsanamira yachiwiri mu Manifesto yanga ndi Job Creation, kapena kuti Ntchito Zokwanira Aliyense, yomwe cholinga chake ndikuthandiza achinyamata 3 million kupeza zintchito mma sector oposa 10 komwe titaikeko ma project osiyanasiyana. Ena ayamba kale kulira kuti zimenezi nzosatheka, koma ine paja nnazolowera kuti ndikati ndimanga 6 lane road, ena ananena kuti nzosatheka; ndinazolowera kuti ndikati M1 ndiisandutsa dual lane ena ananena kuti nzosatheka; ndinazolowera kuti ndikati mtengo wa data mMalawi nditsitsa kuposa maiko onse amu Africa, ena anati nzosatheka zimenezo; ndinazolowera kuti ndikanena**

**kuti CDF ikwera by 7 times, ena ananena kuti nzamisala. Ndiye muzingowayang'ana mukawamva akunena kuti Manifesto yanga siitheka, chifukwa ndi anthu odana ndi chitukuko amenewo.**

**Ndiye kuno kukubwera ma project ankhaninkhani omwe atalembe achinyamata pa ntchito, achina Rumphi-Nyika-Chitipa Road, Chitipa-Ilomba Road, Chiweta-Karonga Road, Livingstonia-Njakwa Road, Rumphi-Bolero-Nyika Road, Lakeshore Road from Nkhatabay-Usisya-Chiweta, Chikwawa-Euthini Road, Lusangazi-Mzuni-Dunduzu Road, yomwe itakhalenso ndi Interchange; Mzuzu City Bypass Road; Mzuzu-Usisya Road. Miseu imenei itsekula mpoto yonse kukha msika otentha. Komanso tiyambitsa Job Creation Fund yothandiza achinyamata kulumikizidwa ku ntchito zomwe ziriko, komanso Youth Innovation Fund yomwe ndayambitsa kale ndi 2 billion in my first term, ndiikamo 5 billion in my second term. Ndiye ndikamati opeza ntchito akwana 3 million sindikunena nthano, koma zinthu zomwe nditachite.**

**Nsanamira yachitatu ndiye ndi Wealth Creation, yomwe cholinga chake nkuchulikitsa zikhwaya mdziko muno. Achinyamata mukunzekere kuzapanga nawo apply program ya Ten-Ten Challenge, yomwe izapereke mpamba okwana 10 million kwacha kwa achinyamata okwana 10,000 omwe ali ndi ma plan opanga bizinesi ya siriyasi osati yongoyesera. Komanso mukonzekere kuchotseredwa misonkho by 10% kuti ndalama yamalipiro izikhala yochulukirapo. Mukonzekerenso kuti magetsi omwe tafikitsa kwa anthu okwana 25% kuchoka pa 11%, tsopano tifikitsa 70%, ndi cholinga choti ma bizinesi ofunika magetsi achuluke. Ndiponso mukonzekere kuti ma units anu amagetsi ndi madzi akatha musanakonzeke kugula ena, muyamba kukhala ndi mwayi ogulako ochepa pangongole kuti bizinesi zanu zisamaime.**

**Nsanamira yachifolo ndi Governance Reform, kapena kuti kuyendetsa boma mwamakono. Ukuku ndiye ndakunga mfundo zothetsa chibwana m'boma. Mwachitsanzo, mu second term yanga mukonzekere kuti ndikuzabhana zomagwiritsa ntchito cash polipira ma**

**services ena ali onse aboma. Ndiye kuti zomalowa mmaofesi aboma ndi cash nkumauzidwa kuti mupereke ziphuphu ndikuthetsa, komanso zomagula katundu mmashopu opanda kupatsidwa risiti yaboma tikuthetsa, chifukwa okugulitsaniwo sitikufuna azikudyerani masuku pamutu. Kukakhala ku mzinda wa Mzuzuko ndiye tikubweretsa zisankho za Meya kuti muzisankha nokha, ndipo ndiamene aziyendetsa ntchito yotukula mzindawo, osati CEO osasankhidwa ndi anthu. Koma pano ndibwerezenso kuti mu Cabinet ndati ndiikamo achinyamata osachepera folo azaka zochepera 35 kukhala nduna za boma, chifukwa achinyamata munandiuza mmene ndimacheza nanu kuti mukufuna mukhale mtika mwenimweni mwa boma.**

**Nsanamira ya chi fayifi ndiye ndi Public Service Delivery, kapena kuti Kulimbikitsa Ubwino Waboma. Mu Manifesto mmenemu ndaikamo ma service 72 atsopano omwe titakhazikitse m'boma. Mmodzi ya iwo ndi ija ya Tsogolo Account yomwe tizitsegulira mwana aliyense obadwa kumene, ndikumusungira ndalamayo mpaka azafike zaka 18 ndikumupatsa ndalamayo**

**itachulukitsidwa kukwana ma million. Ndalamai ena siikuwasangalatsa chifukwa ndi ndalama yoti saazapeza mwayi oyisolola kapena kuiseweretsa. Ndalamai ena siikuwasangalatsa chifukwa akukanika kumvetsa kuti ndizizaiyendetsa bwanji. Koma anthu onsewa ngati saanaziganizepo, nzosadabwitsa kuti akukanika kuzimvetsa. Dziko lomangodya chuma chake ndi dziko lopanda tsogolo. Ndiye mwana obadwa kumene naye ndi mMalawi, ndiye zoti anthu mungomdyela chuma chake nkumusiya munsampha waumphawi ndi ngongole ine ndikuti zithela pa ine. Tikubweretsa Sovereign Wealth Fund ya ndalama za mmigodi, ndalama za ma Carbon Credit, ndalama za ma export a ma Mega Farm, ndipo mwana obadwa mMalawi tizimusungila 500,000 yake yoti wina asangaidye. Ana amenewa akhala ana oyamba kukhala opanda olo mmodzi waumphawi. Ndiye olo otsutsa atsutse chotani, izizi zikuchitika, ndipo malamulo ake tikhazikitsa kuti nonse mudziwe kachitidwe kache, komanso kuti mudziwe njira zonse zomwe tikuika kuti tiletse onse ofuna kupanga abuse program imenei. Ndiye ngakhale anthu apanga phokoso pa nkhani imenei, koma mu Manifestomu ma program alipo ndithu 72 otukula miyoyo yanu, kaphatikizapo**

**CDF yomwe nditakweze kufika 500 million kwacha pa constituency iliyonse.**

**Ulendo tinauyamba limodzi mu 2020 wu, tiyeni tipitilize limodzi mpaka tikafike 2030 komwe kuli dziko lokomela tonse. Musagwedezeke. Musatekeseke. Musanamizidwe. Vuti yanu ndiyomwei chifukwa boma ndilomweli. Ndiye ndi mau amenewa, ndatsekula kampeni yanga kuno kumpoto ndipo ndikhala ndikucheza nanu zonse zomwe titachite limodzi kuno kuti tipitse chitukuko cha kuno ku mpoto patsogolo. Ambuye akudalitseni nonse. Zikomo.**